

# LIU LA NAMIKANGO

## Namikango Mission

Volume 19(2), October 2019



## Kuyenda ndi Kukhala Mwa Mzimu Woyera

Ndikufuna ndikupatseni moni m'malo mwa Namikango. Ndizovuta kukhulupilira kuti chaka chino chikupita nsanga. Nthambi ya za maphunziro pa Namikango yakhala yotanganidwa miyezi yapitayi kuyendera madera osiyanasiyana amene akupanga misonkhano ya misasa. Mutu wa chaka chino wa misonkhano ya misasa wakhala “Kukhala ndi kuyenda ndi Mzimu.” Ifeyo ku Namikango takhala tikulingalira ndi kuphunzira zimene zimatanthauza kukhala ndi kuyenda ndi Mzimu wa Mulungu. Kodi izi zimaoneka bwanji? Kodi tingachite bwanji zimenezi tsiku ndi tsiku? Kodi ndi kusintha kuti kumene kudzachitike m'miyoyo yathu?

Pamene takhala tikufunsa mafunso amenewa, takhala tikuyang'ana ku malemba pa mayankho. Yesu anakamba zambiri zokhudza Mzimu wa Mulungu komanso m'mene amalankhulirana ndi ife, komanso m'mene iye alili Nkhoswe amene amakhala mkati mwathu komanso kuyenda nafe. Paulo akukamba za Mzimu wa Mulungu nthawi zonse, kutifotokozera za m'mene moyo wokhala ndi Mzimu Woyera umakhalira, komanso m'mene ulili ndi mphamvu yosinthira anthu, mipingo, komanso dera la thunthu. Kunena zoon, zikuoneka kuti Mzimu wa Mulungu akuoneka pafupipafupi mu Buku Lopatulika lonse! Kuyambira ndime zoyambirira za Genesis, mpaka ku ndime zomalizira za chibvumbulutso, Baibulo lili lodzala ndi Mzimu wa Mulungu, kugwira ntchito mwa anthu ndi kutitsogolera ife ku chifupi ndi mtima wa Mulungu.

Mu Liu ili, mudzapeza ziphunzitso zingapo za Mzimu wa Mulungu ndi chimene chimatanthauza

kukhala komanso kuyenda ndi Mzimu ameneyu. Muli nkhani yochokera kwa Ryan Hayes, Development Director pa Namikango Mishoni imene ikupita ku chiphunzitso cha Paulo mu Agalatiya 5. Mupezanso nkhani yabwino kuchokera kwa Stanley Mkwanda, Coordinator wa English Bible School pa Namikango imene ikutenga m'mene Baibulo lonse limaonera za Mzimu wa Mulungu komanso zimene zimatanthauza kukhala ndi Mzimuyo. Pomaliza, mupeza kachitidwe ka m'mene zimaonekera kuyenda ndi Mzimu pamene Faith Somanje, wophunzitsa CHE pa Namikango akufotokoza za utumiki wosangalatsa wa CHE komanso zam'mene umabweretsera chiyembekezo ndi kukhazikika kwa anthu komanso maderu m'Malawi yonse ndi maiko ozungulira.

Ndikukhulupilira kuti pamene mukuwerenga Liu limeneli ndi kulingalira pa malemba mkatimu, muphunzira chinachake chodabwitsa chokhudza Mulungu wathu, ndi kufulumizitsidwa kuyenda ndi Mzimu wake. Kuyenda ndi Mzimu wa Mulungu kumatiloleza ifeyo kukhala ndi kuthekera kukafikira mtima wa Mulungu, ndipo pamene tafika pamtima wa Mulungu, timapeza chikondi chozama cha Mulungu pa ife, komanso chikhumbokhumbo chake chozama kuti tikondane wina ndi nzake. Ndikukhulupilira kuti mulimbikitsidwa kukhala ndi Mzimu wa Mulungu, ndi kugawana ndi ena m'mene angachitirensa chimodzimodzi, ku ulemelero wa Mulungu m'Malawi muno!

-Eric Gephart

Pofuna kuti awerengi athu amvetse bwino phunziroli, tatenga mau ambiri mu Chichewa cha lero chopezeka mu Buku loyera (Copyright 1988 by The Bible Society of Malawi).

## Ufulu mwa Khristu Yesu

Cholinga cha nkhaniyi ndi kugwiritsa ntchito mau a Paulo mu Agalatiya 5:13-16 kutikumbutsa kuti mwa Khristu, muli ufulu. Komanso, ndizothandiza kwa Paulo kutikumbutsa ife tonse chimene chimatanthauza kuyenda ndi Mzimu.

Choncho, pamene Agalatiya mitu 1–4 ikhoza kudziwika ngati “moyo kudzera mwa Yesu,” Mitu 5–6 ikhoza kudziwika ngati “moyo mwa Mzimu.” Anthu a Mulungu, Paulo akutero, ndi anthu a Khristu (Akhristu) chifukwa iwo amayenda mwa Mzimu wa Khristu, osati chifukwa amatsatira mndandanda wa malamulo. Agalatiya 5:13-26 akukhudzana ndi kufunikira kwa ufulu polimbana ndi thupi (uchimo). Chikhoza kugawidwa mzigawo zinayi. (1) Paulo akutiitana ku moyo wa ufulu kukulamulidwa ndi thupi (vv. 13–15): kukhala mu ufulu kukutanthauza osakhala mu uchimo koma kukhala mchikondi (cf. v. 6). (2) Iye akubwerezanso maitanidwe ku ufulu pakuitana ku moyo mwa Mzimu kutsutsana ndi thupi (uchimo) (vv.16–18). (3) Iye akutambasula za moyo wathupi (uchimo) (vv. 19–21). (4) Akutambasulanso za moyo wa Mzimu (vv. 22–26). Zigawo zinayi zimenezi zimatithandiza mutu umenewu momveka bwino.

### 1. Ufulu mwa Khristu (vv. 13-15)

Paulo akuyamba mutu 5 pakunena kuti: “Khristu anatisandutsa mfulu” (Agalatiya 5: 1...). Mwa Khristu, timamasulidwa kuchoka ku: uchimo onse, kulakwa konse, kumasulidwa ku mantha owopa Mulungu (kuopa kulangidwa), kuchoka kukutsata malamulo a Chiyuda kapena malamulo amtundu wina uliwonse opangidwa ndi munthu, kumasulidwa kuzimphamvu ndi maulamuliro ndi zina (Akolose 2..Agalatiya 3, Aroma. ). Mwachidule, kakhaliwe kamoyo mwa Khristu ndi ufulu – osati kumangidwa ndi malamulo akunja kwa thupi kapena malamulo ena koma kuyenda ndi Mzimu wa Khristu mwa ife, kutitsogolera tsiku ndi tsiku. Kwa Paulo, cholinga cha ufulu ndi chikondi (Agalatiya 5...). Chifukwa chimene tinamasulidwira sikuti basi tikhale pansu kunyumba

### Agalatiya 5:13-16

Pakuti adakuitanani inu, abale, mukhale mfulu; chokhacho musachite nao ufulu wanu chothandizira thupi, komatu mwachikondi chitiranani ukapolo. Pakuti mau amodzi akwaniritsa chilamulo chonse ndiwo; Uzikonda mnzako monga udzikonda iwe mwini. Koma ngati mulumana ndi kudyana, chenjerani mungaonongane. Koma ndinena, Muyendeyende ndi Mzimu, ndipo musafitse chilakolako cha thupi.

kwathu ndi kumaonera mpira kwinaku tikusangala ndi uchimo wathu umene unakhululukidwa, koma kuti tikathe kuonetsa ufulu wathu pakukhala moyo omasuka ku mantha, udani, kusakhululukidwa komanso kukonda anthu amene azungulira tsiku ndi tsiku.

Anthu ambiri amachita mantha ndi ufulu chifukwa amaganiza kuti zimatanthauza kuti “tili ndi ufulu omachimwa mu njira iliyonse imene tingafunire”. Ngakhale kuti mukhoza kusankha uchitsiru ndi ukapolo wa uchimo onse umene mungafune. Koma ngati mungachite, mukhoza kukhala kuti mukungoonetsa kuti simukumvetsa ufulu komanso kuti simuli a ufulu. Kusankha kuchimwa ndi kusankha ukapolo wa uchimo. Kodi izi ndi zimene mumakhumba kwambiri? Kodi mumakhumba kuyenda ndi uchimo kapena kuyenda ndi Mzimu? Chisankho ndi chanu.

Kagwiritsidwe ntchito ka ufulu kamene Paulo akufuna kutionetsa ife ndi njira ya moyo (yoyenda ndi Mzimu wa Khristu) imene imatithandiza kusankha chikondi m'malo mwa udani, nsanje, mkwiyo ndi chigololo. Indedi, kagwiritsidwe ntchito ka ufulu ndi kukwaniritsa lamulo lonse limene laphatikizidwa pamodzi monga “kukonda mnansi wako monga udzikondera iwe mwini” (Agalatiya 5:14). Kukhala ndi zilakolako za kuthupi monga chilakolako cha chigololo, udani, miseche ndi mkwiyo si kusankha ufulu, ndi kusankha ukapolo. Kodi amene amasankha kunena miseche anthu ndi mfulu? Ayi, ali mu ukapolo ku zilakolako za udani, kunama, chilango ndi kuweruza ena. Kukhala ndi chikondi

kokha – kuona anthu monga Mulungu amawaonera ndi kuchita mwa chifundo kwa anthu ena – ndiye ufulu weniweni. Yesu amationetsera m'mene tingakhalire mu ufulu pamene akuti “kondani Mulungu, Kondani mnansi wanu monga inu” (Luka 10:27; Mark 12:31). Tsopano mukhoza kuona kuti ndili ndi ufulu opanga chinachake ngati chili chodalitsa mnansi wanga ndipo ndi chochitika chimene chikuonetsera Yesu Khristu kwa ena. Ufulu = kukhala mwa Khristu = kumene kuli kukhala ndi Mzimu wa Khristu = kumene kuli kuonetsera chifundo, ndi chikondi cha Yesu. Kodi mukukhala mu ufulu wa Khristu lero? Kodi moyo wanu umaonetsera zofuna za Yesu, chifundo, kwa anthu onse?

## **2. Ufulu ndi kuyenda ndi Mzimu wa Khristu (vv. 16-18)**

Paulo akutithandiza kumvetsetsa kuti thupi lathu limagwira ntchito kuti likapindule ilo lokha komanso kuti lisungike ilo lokha. Timadzikweza tokha kuposa anthu ena. Ichi n'chifukwa chakuti aliyense wa ife amakhala okhudzika ndi za moyo wake basi, chakudya chathu, kuchita bwino kwathu komanso kutchuka kwathu. Monga anthu, timakonda kudzisamalira ife eni tisanayambe kuganiza za ena. Izi ndi zolinga zokhudzana ndi thupi (uchimo), kutsutsana ndi Mzimu. Chifukwa? Chifukwa Mzimu wa Khristu amapereka choonadi chakuti Mulungu amatikonda ifeyo, kuti sitikuyenera kuopa Mulungu (kuopa kulangidwa) kapena munthu wina aliyense, kuti kuona anthu ena monga momwe Mulungu amawaonera (ndi chifundo, chikhululukiro ndi chikondi) umu ndi mmene Yesu anakhalira.

Komanso china chimene chimagwirizana ndi ntchito za thupi ndi kufuna kutsata malamulo ndi Chilamulo. Ndizosavuta kutsata malamulo kusiyana ndi kuyenda ndi Mzimu. Chifukwa ndi malamulo, zochitika zimaoneka. Wina akhoza kudziyerekeza ndi anthu ndi kuona amene akutsata malamulo komanso sakutsata ndi ndani. Timadziona ifeyo eni monga otsatira malamulo abwino, choncho timaweruza anthu ena pakusatsata malamulo monga ife tichitira. Koma “Ngati Mzimu akutsogolerani, simuli omvera lamulo” (Agalatiya 5:18). Choncho sitili pansu pa Lamulo monga a Khristu. Sitili pansu pa lamulo

lililonse, kupatula lamulo la chikondi (tchulani). Chikondi cha Mulungu pa “ochimwa” sichidalira pakutsata malamulo. Timapulumsidwa mwa chisomo kudzera m'chikhulupiliro (Aefeso 2v8). Chifundo chenicheni ndi chikondi ndi zimene talandira, ngakhale pamene sitinayenere kapena kutsata malamulo (Aroma. 5:1-5). Tsopano, kupereka chikondi kwa wina aliyense monga Mulungu waperekera kwa ife ndi chimene Mzimu wa Khristu amayesera kuchita mwa ife.

## **3. Kumvetsetsa ukapolo wa zokhumba zathupi (vv. 19-21)**

Koma mavuto a kuthupi si “machimo akuluakulu” okha amene timakonda kutchula. Timakonda kukamba za “machimo akuluakulu” amene ali owonekera kachitidwe kake: kupanga chigololo, kuledzera, kupha winawake, kapena kuba. Amenewo ndi machimo ndithu, koma Paulo akunena momveka bwino kuti “kukhala kuthupi” ndi kuphatikizanso: kudana, miseche, ufiti, kupembedza mafano, nsanje, mkwiyo pa wina aliyense komanso kugawa maubale. Ngakhale a Khristu, kodi ifeyo sitikhala ndi mkwiyo kapena miseche kapena udani mu mtima mwathu, ngati tilidi owona mtima? Kodi ndi angati aife amene anakhumudwitsidwa ndi winawake ndipo mkukana kuwakhululukira? Ukunso ndi kukhala mu thupi. Amene akukhala ndi zolinga ndi ntchito zimenezi sakupeza “Ufumu wa Mulungu”. Ufumu wa Mulungu ndi, m'mau a Yesu, mwa ife pafupi ndi ife, mozungulira ife? Izi zikutanthauza kuti anthu amene akusankha ukapolo wa thupi, sakusangalala ndi ufulu umene umabwera kudzera mchifundo, chikondi ndi chikhululukiro.

## **4. Chipatso cha kuyenda ndi Mzimu (vv. 22-26)**

Pomaliza, Paulo akufotokoza za moyo osiyana umene tikuyenera kukhala m'mene ungakhalire. Izi ndi zotsatira zakukhala ngati Yesu, kudzadzidwa ndi Mzimu yemweyu wa Khristu amene analola Yesu kuti adziona anthu m'mene Mulungu amawaonera – ndi chisoni, chifundo ndi chikondi. Ndizofunikira kunena chimene chisali Chipatso cha Mzimu. Si “kulankhula m'malilime, kapena kunenera, kapena kuona masomphenya, kapena kulankhula ndi nzeru” (1Akorinto

13:1-5)”. Chipatso cha Mzimu ndi zochita monga: chikondi, chimwemwe, mtendere, kudekha, kukoma mtima, ubwino, kudekha ndi kudziletsa. Kodi moyo wanu umaonetsera zolinga ndi zochita zimenezi? Kapena mukukhalabe ndi mkwiyo, Kusakhululuka, udani,nsanje kwa anthu ena?

Koma “iwo a Khristu Yesu adapachika thupi ndi zokhumba zake, ndi zilakolako zake.” (Agalatiya. 5:24). Iwo amene “ali a Khristu Yesu” ndi amene alandira uthenga wabwino wa chikondi cha Mulungu ndi chikhululuko ndipo apanga chiganizo mwa chikhulupiliro kuti akhale “mwa Khristu”. Anthu amenewo “afa ndi kuukitsidwa limodzi ndi Khristu” (Aroma. 6), ichi ndi chimene ubatizo umaonetsera – kumizidwa kuli ngati kufa ndi kutuluka m’madzi ndi moyo watsopano – kuukitsidwa ndi Khristu. Komanso, Paulo akuti, “chifukwa Khristu anafera onse, onse anafa...” (Akolose 3:1-3). Kwa Paulo, tinafa kale chifukwa tinavomera kuti Mulungu amatikonda posatengera thupi lathu. Tsopano tili “zolengedwa zatsopano”, “zoyanjanitsidwa kwa Mulungu kudzera mwa Yesu (2 Akorinto 5:16-22). Koma! Ngakhale tili oyanjanitsidwa kwa Mulungu, ndipo tili “mwa Khristu, tikuyenerabe kumayenda ndi Mzimu tsiku ndi tsiku, chifukwa tilibe ndi mkwiyo ndi udani ndi nsanje mmitima yathu. Choncho, Paulo akuti: thupi lanu linafa kale ndi Khristu, ndipo munaukitsidwa ndi Khristu, choncho chitani motero! Chitani monga kuti izi ndi zoono lero. Koma ambiri sakuchita ngati izi ndi zoono. Ndi Mzimu yemweyo wa Khristu mwa ife, tiyeninso tipereke chisomo chomwecho kwa anthu otizungulira. Zingatheke bwanji kusaonetsera Mzimu yemweyo ali mwa ife ndi kuyenda ndi ife? Monga Mzimu wa Khristu anatiululira kudzera mwa m’mau a Khristu: “adzakudziwani kuti ndinu a Khristu ndi chikondi chanu” (Yohane 13:35).

1. Ndi mau a Paulo alimwambamu, mwakhala molingana ndi thupi mwezi watha (udani, Kusakhululuka, nsanje, miseche, magawano, chikhumbokhumbo chonyasa kapena kuledzera)?
2. Lero, mukukhulupilira kuti zokhumba zanu zafa ndipo kuti mwaukitsidwa ndi Khristu ngati wolengedwa mwatsopano?

3. Kodi mungayambe bwanji kuchita chipatso cha Mzimu m’moyo wanu lero?

-Ryan Hayes

## Ntchito ya Mzimu Woyera

“Pachiyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi. Dziko lapansi ndipo linali lopanda kanthu; ndipo mdima unali pamwamba pa Nyanja, ndipo Mzimu wa Mulungu unali kufungatira pamwamba pa madzi” (Genesis 1:2). Anthu ambiri timasausika tikamaganizira za Mzimu Woyera komanso Mzimu wa Mulungu. Mafunso amabwera kuti kodi Mzimu wa Mulungu ndi Mzimu Woyera yemweyu? Apa tikudzindikira kuti dziko lisanalengedwe, Mzimu wa Mulungu unali utayamba kale kugwira ntchito yofungatira. Tikamati kufungatira tizikhala ndi chithuzithuzi cha nkuku yomwe imafungatira madzira ndi chiyembekedzo kuti pakudusa kwa nthawi patuluka kanthu. Mzimu wa Mulungu kapena kuti Mzimu Woyera anatenga nawo gawo pa chilengedwe chadziko ndi zinthu zokhalamo. Pakulengedwa kwa munthu, panamveka mau “tipange munthu mchifaniziro chathu, monga mwa chikhaliidwe chathu” (1:26). Mau amenewa akuonesa kuti chiganizo cholenga munthu chinatuluka kuchokera mu umodzi wa Umulungu ngakhale sipakuoneka mwa chindunji.

Tikamawerenga chipangano chakale timaona kuti Mzimu wa Mulungu unagwira ntchito kuzera mwa aneneri, mafumu komanso anthu wamba cholinga chofuna kuchenjedza komanso kupulumutsa anthu ake akachoka pamaso pake. Mzimu wa Mulungu umagwiranso ntchito mwa anthu ndi cholinga chofuna kukwaniritsa ntchito yomwe Mulungu amafuna kuti igwirike kwa kanthawi. Mubuku la Oweruza tapatsidwa chitsanzo chomwe Mzimu wa Mulungu unaonekera kwa Otaniyeli kuti atsogolere ana a Israyeli kukamenya nkondo ndi mfumu ya Mesopotamiya atamva kulira kwa ana a Israyeli chifukwa cha zochimwa zawo (Oweruza 3:10). Apa titha kuona kuti Mzimu wa Mulungu umathandiza kupulumutsa anthu ake akalira kwa Iye ndipo amapulumutsidwa. Koma pakudusa kwa nthawi, Mulungu anapereka lonjezo kuti Mzimu

udzafika pa aliyense nadzakhala ndi aliyense. Yoweli anati. “Ndipo kudzachitika mtsogolo mwache, ndizatsanulira mzimu wanga pa anthu onse.....” (2:28). Cholinga ndichakuti Mzimu Woyera azakhale mwa aliyense ndi kumupanga munthu kukhala monga momwe Mulungu anafunira kuti munthu akhale pachilengedwe chake. Zonsezi zinadalira kubwera kaye kwa Yesu Khristu. Mu mauthenga abwino atatu oyambilira, zikuoneka poyera kuti cholinga chake kunali kufuna kuonesera Yesu osangoti monga mphunzitsi wa Mzimu Woyera, koma munthu wodzazidwa ndi mzimu monga momwe aneneri analoselera. Tonse tikudziwa bwino kuti malo ambiri momwe Yesu akupezeka mma uthenga

abwino Mzimu woyeranso akupezeka monga, pakubadwa kwake, kubatidzidwa, kuyesedwa kwake, kulalikira kwake koyamba, mmene amatulutsa ziwanda komanso pa mtanda paja.

Pakuyang’ana monsemu titha kuona kuti mabuku authenga wabwino amafuna kuonesa kuti Yesu Khristu moyo wake komanso utumiki zimasogodzedwa ndi Mzimu Woyera ndipo Mzimu Woyera anali mwa Iye.

Mulungu anabwera kuzakhala ndi anthu kudzera mwa Yesu Khristu (Akolose 1:19). Yesu pokhala munthu yemwe anabwera ndi cholinga, inakwana nthawi yake kuti akwaniritse cholingacho ndi kubwelera kwa Atate. Chimenechi chinabweretsa mantha pakati pa ophunzira ake omwe amalimba mtima ndi kupezeka kwa Yesu pakati pao. Iye anadziwa zomwe zimayenda mmitima ya ophunzira ake ndipo anafuna kuwalimbikitsa. Yesu anati, “mtima wanu usavutike, khulupilirani Mulungu, khulupilirani insenso. Mnyumba ya Atate wanga alimo malo okhala ambiri. Ngati sikudali kutero, ndikadakuuzani inu; pakuti ndipita kukakukonzerani inu malo” (Yohane 14:1- 2). Ophunzira anaonesa kuperewera kwao kudzera mmafunso omwe amafunsa komanso machitidwe awo. Koma Yesu anali akudziwa kuti sawasiya okha. Nthawi zambiri ifenso timakhala ndi mantha

chifukwa cha zinthu zambiri zomwe timakumana nazo mmoyo wanthu wa siku ndi siku. Matenda akafika pakhomo timadera nkhawa, tikamasowa zinthu zofunika mmoyo uno timadandaula kwambiri, okonedwa anthu akatichokera pakati pathu timasweka mtima monga anthu kumaona ngati tili tokha.

Chimenechi Yesu anachiona kale pakati pa ophunzira ake ndipo Iye anapempha Atate kumwamba kuti alowelerepo. “Ndipo Ine ndidzapempha Atate, ndipo adzakupasani inu Nkhoswe yina, kuti akhale ndi inu ku nthawi zonse, ndiye Mzimu wa choonadi...” (Yohane 14:16 – 17). Pamene Yesu akunena kuti

### Yohane 14:16-17

Ndipo Ine ndidzapempha Atate, ndipo adzakupatsani inu Nkhoswe ina, kuti akhale ndi inu kunthawi yonse, ndiye Mzimu wa choonadi; amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona Iye, kapena kumzindikira Iye. Inu mumzindikira Iye; chifukwa akhala ndi inu nadzakhala mwa inu.

adzakupatsani inu Nkhoswe ina, ndichachidziwikire kuti ndi ofanana ndi Iye kuti azakwaniritse kugwira ntchito yomwe Iye amagwira. Yesu akanapanda kupempha Atate kuti atumize Nkhoswe, ophunzira ake

akanakhala amasiye chifukwa akanasowa kopeza thandizo pamene asausika. Tonse timadziwa bwino kuti ana omwe alibe munthu owayanganila pamene makolo awo amwalira amakhala amasiye kotero amakhala ndi nkhawa komanso osasangalala. Koma pamene wina wapezeka kuwasamalira amalimba mtima. Yesu anawapemphera ophunzira Nkhoswe yoti iziwasamalira ifenso lero pokhala akhristu tikusamaliridwa ndi Nkhoswe yemweyo. “Koma Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma mdzina langa, Iyeyo adzaphunzitsa inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu” (vs. 26). Pali ntchito zina zomwe Mzimu Woyera (Nkhoswe) amagwira mwa ife. Yesu wafotokoza kuti Iye adzaphunzitsa, cholinga chophunzitsa ndikupereka chidziwitso kuti munthu akhale odziwa choyenera kuchichita pa nthawi yake. Mwa ife tokha sitingathe kudziwa china chili chonse tikusowekera Mzimu Woyera atiphunzitse kuti tidziwe chifuniro cha Mulungu ndi chani. Nthawi zambiri timapanga chifuniro chathu kusiya cha Mulungu mwakutero timasusana ndi Mulungu. Ophunzira a Yesu anaphunzira zambiri pa nthawi anali ndi Iye ndipo sakanatha

kukumbukira kalikonse ndi chifukwa chake, anasowokera Mzimu Woyera kuti adziwakumbutsa.

Yesu amadziwa kufooka kwathu, patokha sitingakhale ndi kulimbika mtima koma tisowekera Mzimu woyera kuti azikhala nafe nthawi zonse. Mavuto omwe timakumana nawo monga kunyozedwa, kunamiziridwa, kuzuzidwa chifukwa cha chipembedzo, umasiye, kusefukira kwa madzi, kusalidwa, mabanja kusayenda bwino, kuponderedzedwa, mwa umunthu wathu sitingathe kupilira koma Mulungu kudzera mwa Mzimu wake yemwe amakhala mwa ife amatithandiza kuti tipambane mayesero kapena mavuto ngati amenewa akabwera mmoyo mwathu. Anthu ena mavuto akawakulira amapeza njira zina kufuna kuti ayiware mavuto awo monga kuledzera mowa ngakhalenso kumwa mankhwala odzunguza bongo. Koma ife tidzindikire kuti Mzimu yemwe ali mwa ife amatithandiza kuti tipambane kapena tiduse mu nthawi zovuta zomwe zimabwera mmoyo wathu. Pokhala akhristu tinayenera kumayenda komanso kukhala mwa Mzimu chifukwa imeneyi ndi njira yokhayo yomwe tingakhale ndi moyo opambana. Nthawi zonse umunthu wathu umafuna kutilamulira kuchita zinthu zotsusana ndi Mzimu koma Paulo anakumbutsa akhristu ku dera la Galatiya. “Ngatitu tiri ndi moyo ndi Mzimu, ndi Mzimunso tiyende” (Agalatiya 5:25). Pamenepa tikuona kuti anthu ambiri timakhonza kuvomera kuti ndife ake akhristu Yesu koma makhalidwe amoyo wathu amaoneka kuti akulamuliridwa ndi umunthu wathu osati Mzimu Woyera.

Nthawi zambiri tikafuna kupanga chinthu, Mzimu amatiuza kuti ayi usapange chimenecho, koma vuto lake satana ndi ochenjera amationetsara ubwino omwe umapezeka mu zinthu zomwe thupi limafuna osaonesa mavuto ake. Ndipo thupi lathu limapambana pamene timvera zofuna za moyo wathu. Zikavuta mpamene nzeru zimabwere, anthu ambiri agwa mmavuto osiyanasiyana chifukwa chomvera umunthu wao. Kunafunika kuzindikira kuti zokhumba za thupi lathu zimasusana ndi Mzimu. Mwaife tokha sitingathe. Paulo pokhala munthu naye anaona nkondo yomwe imakhala mwa munthu aliyense. “Pakuti chimene ndichita sindichidziwa; pakuti sindichita chimene ndifuna,

koma chimene ndidana nacho ndichita ichi” (Aroma 8:15). Nthawi zonse mumakhala kulimbana mkati mwathu ndipo ngati sityenda ndikukhala mwa Mzimu Woyera tidzalephera chifukwa mwaife tokha ndife ofooka. Mzimu Woyera Sali kutali nafe ali mwa ife, funso lotithandiza mkumati, “Kodi simudziwa kuti muli kachisi wa Mulungu, ndi kuti mzimu wa Mulungu agonera mwa inu”? (1 Akorinto 3:16). Zinafunika kuti funso limeneli tizilimva m’mutu mwathu nthawi zonse kuti tizikumbutsidwa ndikudzindikira kuti matupi anthu ndi opaturika chifukwa Mzimu Woyera amagonera mwa ife ndipo oipayo akafuna kutinyengelera ife tidzimvera Mzimu Woyera. Paulo anamkumbusa Timoteyo kuti “pakuti Mulungu sanapatsa mzimu wa mantha, komatu wa mphamvu ndi chikondi ndi chidziletso” (2 Timoteyo 1:7). Ngati Mkhristu aliyense atadzindikira kuti mwa iye muli Mzimu wa mphamvu, omwe Mulungu anatipatsa tidzakhala akhristu olimba ndipo sitingamatengeke ndi ziri zonse chifukwa Iye adzikhala olamulira moyo wathu.

-Stanley Mkwanda

## **(CHE) Ikudalitsa Miyoyo ya Anthu**

CHE ndi umodzi mwa mautumiki amene Mishoni ya Namikango ikuchita ku Malawi komanso maiko oyandikira. Cholinga chake chikuchokera pa Yohane 10:10 m’mene Yesu akufotokozera anthu za kukhala ndi moyo wochuluka. CHE ili ndi zigawo zosiyanasiyana zimene zimakwaniritsidwa, chimodzi motsatizana ndi china kutengera m’mene choyambacho chathekera mkukwaniritsidwa kwake (ngati tcheni). CHE imalunjika pakuthandiza anthu kuzindikira choonadi chokhudza kukhala kuthupi komanso umunthu wauzimu kudzera ku maphunziro a Baibulo komanso ku zochitikachitika, komanso kuwathandiza kufalitsa uthengawu kwa anzawo (Marko 12:31 ndi 2 Timoteo 2:2). Mishoni ya Namikango imapereka nzeru, luso, ndipo nthawi zina zipangizo zimene zingathandizire anthu amene aphunzitsidwa kukachita zimene aphunzira; zipangizozi ndi monga zophunzitsira komanso ophunzitsa. CHE imalunjika pa kupewa osati kuchiza, kaganizidwe

ka umwini osati kudalira, kutenga gawo lathunthu osati oyang'anira, utsogoleri wa uzimu, kukhazikika, ndi chitukuko osati thandizo komanso kuchulukitsa.

Pakupitiriza kulimbikitsa maubale ndi miyoyo ya anthu m'Malawi ndi maiko oyandikira, dongosolo la CHE laphunzitsa anthu ambiri kupatula alimi 85 otsogolera amene dongosololi lagwira nawo ntchito chaka chino. Kulimbikira kwathu sikunapite padera, monga malemba anenera mu Mateyu 25:14-30, taona anthu atatu mwa alimi athu otsogolera komanso ophunzira, ena anachita bwino ndi ma talente amene timapereka kwa iwo, ena anachita bwino zedi ndipo ena sanachitepo kanthu koma kumangonyinyilika popanda kanthu. Atumiki abwino adzakhulupilidwa ndi dongosolo lopitilira kuti akathe kupitiliza kuchita ntchito yabwino imene akuchita ndi kuperekanso lusolo kwa miyoyo yambiri.

Cholinga chenicheni chimene tinakhalira ndi alimi otsogolerawa chinali kukhala ndi ziphona zakudera zimene zingakathe kuphunzitsa ndi kuthandiza ena mumpingo ndi mudera ndi magawo onse a CHE. Awa ndi amene amayenera kukhala atsogoleri, kukhala opereka uthenga oyambirira pa za ntchito ya CHE ndipo ali choncho. Kulima m'Njira ya Mulungu ndi gawo limodzi la ntchito ya CHE imene imalunjika pakubwezeretsa ubale pakati pa anthu ndi chilengedwe (kubwerera ku Edeni). Ubale umenewu ukhoza kukwaniritsidwa pokhapokha pamene anthu amvetsetsa chiyambi cha moyo komanso zochitika zokhudza moyo. Ntchito zambiri za anthu zimalunjika pa kuteteza chakudya ndi kupeza ndalama, koma amaiwala kuchilikiza kwa zinthu ziwiri zimenezi. Ichi ndi chifukwa chake anthu adula mitengo mosasamala kuti apeze ndalama, agwiritsa ntchito feteleza ndi mankhwala kuti akolole chakudya chimene chidzawatengere ku chaka china chotsatira cha ulimi. Kulima m'Njira ya Mulungu, mu zaka ziwiri zapitazi yaonetsera kwa ife komanso alimi otsogolerawa amene anakhazikika bwino mu dongosololi kuti likhoza kuthandiza makomo ambiri kukhala ndi chakudya chokwanira komanso kugulitsa chotsala kuti akhale okhazikika pa chuma. **Taganizani malo okula mamita 50 koma opanda chonde mkukololamo matumba 20**

**olemera 50kgs ya chimanga mu chaka choyamba chogwiritsa ntchito manyowa a kompositi!** Kulima m'Njira ya Mulungu kumalimbikitsa kugwiritsa ntchito zipangizo zopezeka mosavuta komanso zachilengedwe; izi zachepetsa zipangizo zolowa ku ulimi koma zachulutsa zokolola. Izi zimapititsa patsogolo chonde mnjira zambiri; kubwezeretsa kaonekedwe, kubwezeretsedwa kwa chonde, kuika pa mlingo wabwino wa katenthedwe ka donthi, kulinganiza mchere wa mu nthaka, kubweretsanso moyo mu dothi ndi kukhazikitsa chinyontho. Izi zimachitika pakutsata mfundo zisanu za Kulima m'Njira ya Mulungu; Kusatembenuza nthaka, ulimi wa manyowa, kuphimbira nthaka, kulima mbewu mwakasinthasintho ndi ulimi obzala mitengo. Mfundo zonsezi zimatsogozedwa ndi malemba kulimbikitsa maziko a zonse.

CHE yathandiza kwambiri pakumanga kuthekera kwa kuthupi komanso pa chuma kwa anthu pafupifupi 160 pakusintho m'mene amaganizira komanso m'mene amaonera zinthu zimene zawazungulira. Izi zawasinthanso moyo wawo wauzimu, kuwapatsa kuthekera kuona anthu amene sali mu mpingo monga anthu amene alandiranso chisomo koma sakuchizindikira. Anthu ochuluka amene sali mamembala a Mpingo wa Khristu anailandira pologalamuyi ndipo akugwira ntchito mogwirizana ndi alimi otsogolera, mpaka ena anayamba kupita ku mpingo kusonyeza kuthokoza kwao pa chiphunzitsa chokhudza magawo onse a moyo wa munthu cha dongosolo la CHE. Iyi ndi nkhani yabwino! Pologalamuyi yathandizanso kupititsa patsogolo mchitidwe opereka kudzera mziphunzitsa zake, (kupereka kumadalitsa koposa kulandira Machitidwe Atumwi 20:35). Mu mdalitso uliwonse umene Ambuye wapereka, anthu amalangizidwa kuti atsate malemba pakupereka ku mpingo komanso kwa aumphawi. Pafupifupi alimi okwana 25 achitira umboni kuti Mulungu wachita zinthu zazikulu pa iwo atapereka ku mpingo komanso kwa aumphawi. Tikukhulupilira kuti ngati chizolowezi choperekachi chitafalikira kwa anthu onse chidzabweretsa kusintho ku mpingo, kudera, komanso ku dziko. Zidzathandiza (monga chayamba kale) kumanga mzimu odzidalira ndi kupanga madera komanso mipingo kuti zikhale

zodzidalira.

CHE yathandiza kumanga ndi kulimbikitsa ubale wabwino pakati pa Mishoni ya Namikango ndi mipingo ya Khristu m'Malawi, gawo la Mozambique ndi gawo lina la Zambia kudzera mu pologalamu ya mpingo ya HIV/EDZI, ndi maphunziro angapo a ophunzira ndipo izi zalimbikitsa kupezeka kwa uthenga wa HIV/EDZI ku mipingo. Kupatula kulimbikira konseku, pali zambiribe zoti zichitidwe komanso mipingo yambiri ndi madera oti afikiridwe, tikukhulupilira kuti kudzera ku kuchulukitsa zonse zidzakhala zotheka. Tikukhulupiliranso kuti moyo wosatha ndi wotheka kudzera mu dongosolo la CHE (Kufikira madera ndi uthenga wa umoyo; ku uzimu komanso kuthupi).

Zonse kuziika pamodzi, CHE yathandiza pakuphunzitsa anthu kumvetsa ubale wawo ndi anthu ena, chilengedwe cha Mulungu komanso Mulungu mwini. Ndikuthandiza anthu kuzindikira mavuto amene amayambitsidwa ndi ifeyo anthu kuyambira nthawi ya uchimo mu Edeni. Kuyesetsa konse kwakhala kuli kopereka nzeru kwa anthu ochuluka m'mene tingathere kuthandiza kupititsa patsogolo chilengedwe cholinga anthu akhale ndi zinthu kuti akhale ndi moyo wabwino kuti akathe kutumikira Mulungu bwino. Ndi kulimbikitsa chikondi pakati pa mipingo ndi madera. Tikukhulupilira kuti kudzera kwa adindo amene tawaphunzitsa ndi ena amene tiwaphunzitse, tidzatha kufikira anthu ambiri. Tikuthokoza anthu onse amene amathandiza utumikiwu kuti upite patsogolo, ulemelero ukhale kwa Mulungu nthawi zonse.

-Faith Lewis Somanje

## Zolengeza

### Maphunziro

- Zokonzekera za maphunziro a Bible omwe akuyembekezeka kuyambanso kuno ku Namikango Bible School ziri mkati. Abale ndi alongo tikukupemphani kuti mupitilize kudikilirabe zonse zikakonzeka tidzakudziwitsani.
- Tidzakhala ndi msonkhano wa atsogoleri a mpingo pa Chinsapo Church of Christ pa 9

November, 2019. Atsogoleri onse a m'boma la Lilongwe komanso ma boma oyandikira muli oyitanidwa. Maphunzirowa adzakhala a tsiku limodzi kuyambira 8 koloko mmawa kufikira 3 koloko masana. Pofuna kudziwa zambiri mungathe kufunsa atsogoleri a pa Chinsapo kapena m'bale Sam Tambala pa nambala iyi 0884 195 459.

### Msonkhano waukulu wa mchigawo cha kummwera kwa Africa

- Msonkhanowu chaka cha mmawa ulikonso. Abale ndi alongo omwe akufuna kupita ku Bulawayo akupemphedwa kulipira ndalama yolembetsa yokwana K35,000 ndi K65,000 yoyendera. Ndalama zonse pamodzi zikukwana K100, 000 munthu mmodzi. Tiyeni tilipile nthawi idakalipo kuti zokonzekera zikhale zosavuta.

### Odwala

Tiyeni tipitilize kuwapemphelera abale awa omwe akudwalabe.

- Bambo Misomali omwe ndi mlaliki a pa Zomba Central Church of Christ
- Bambo BS Mbewe omwe amakhala ku Liwonde m'boma la Machinga.
- Bambo John Katete ku Chingale m'boma la Zomba.
- Bambo Bvuta omwe ndi mlaliki ku dera la Likangala Zomba East.

### Otsiya

- Alaliki a Tsonga anamwalira pa 31 August ndipo analowa mmanda pa 1 September, 2019. Iwo amachokera mu boma la Chikwawa.
- Bambo Matchado omwe anali mlaliki mboma la Chiradzulu anamwalira pa 14 September, 2019, ndipo anaikidwa mmanda pa 15.